# YESU KRISTU

*'Chonde, ngati nkotheka malizani*

*kuwerenga kabukuka.*

*Zikomo.'*

**Mau oyamba**

Ngakhale anthu ali ndi zikhulupiriro zosiyana-siyana  pa Yesu Kristu, koma kodi Baibulo liti Yesu anali yani?

**<u>GAWO 1</u>**

**MMODZI WA ATATU?**

<u>Umboni wa chikhulupiriro cha umodzi wa atatu wa Yesu mBaibulo;</u>

# MATEYU 28:19

# *“ Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m’zina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:”*

Koma ngakhale izi zili chonchi, pali mavesi ena mBaibulo omwe ndiochuluka omwe akutsutsana ndi chikhulupirirochi.

<u>Umboni otsutsana ndi chikhulupirirochi;</u>

# MATEYU 3:11

# *“Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma iye wakudza pambuyo panga, ali wamphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto”*

# MACITIDWE 1:5

# *“Pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri.”*

Kuonjezera apa, Yesu anali akuwaphunzitsa anthu za umodzi wa Mulungu osati utatu wa Mulungu.

**MARKO 12:28-31**

***" ...Yesu anayankha, kuti Lamtsogolo ndili, Mvera, Israyeli; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi..."***

**MATEYU 4:10** ***"Pomwepo Yesu ananena kwa iye, Coka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzamlambira."***

Zonga zomwezinso zikupezeka pa

**DEUTRONOMO 6:4**

***"Imvani Israyeli; Yehova Mulungu wathu ,Yehova ndiye MMODZI."***

**EKSODO 20:3**

***"Usakhale nayo Milungu yina koma Ine ndekha"*** ndi ena monga **YESAYA 44:6 ndi YESAYA 45:21-23.**

**GAWO 2**

## MULUNGU AMENE?

Umboni wa Umulungu wa Yesu;

**1-Anadzala ndi Mzimu Woyera.**

Ngati Yesu ali Mulungu kamba kodzazidwa ndi Mzimu Woyera, palinso anthu ena omwe anadzazidwa ndi Mzimu Woyera koma satengedwa ngati milungu.

Barnaba anali odzala ndi Mzimu Woyera,

# MACITIDWE 11:24

***"Chifukwa anali munthu wabwino ndi wodzala ndi Mzimu Woyera ndi cikhulupiriro: ndipo khamu lalikulu lidaonjezeka kwa Ambuye."***

Elizabeti nayenso anadzazidwa ndi Mzimu Woyera,

# LUKA 1:41

***"Ndipo panali pamene Elizabeti anamva kulankhula kwace kwa Mariya, mwana wosabadwayo anatsalima m'mimba mwace; ndipo Elizabeti anadzazidwa ndi Mzimu Woyera"***

**2-Anadzala ndi Mzimu Woyera anakali m'mimba mwa amai ake.**

Yohane nayenso anali odzazidwa ndi Mzimu Woyera asanabadwe,

# LUKA 1:15

***"Pakuti iye adzakhala wamkulu pamaso pa Ambuye, ndipo sadzamwa konse vinyo kapena kacasu; nadzadzazidwa ndi Mzimu Woyera, kuyambira asanabadwe."***

**3-Amachulukitsa chakudya.**

Eliya ndi Elisa nawonso amachulukitsa chakudya,

# 1-MAFUMU 17:16

***"Mbiya ya ufa siidatha, ndi nsupa ya mafuta siinacepa, monga mwa mau a Yehova amene ananenetsa Eliya."***

# 2-MAFUMU 4:44

***"Potero anawagawira, nadya, nasiyapo, monga mwa mau a Yehova."***

**4-Amachidza akhate.**

Elisa nayenso amachidza akhate,

# 2-MAFUMU 5:14

***"Potero anatsika, namira m'Yordano kasanu ndi kawiri, monga adanena munthu wa Mulunguyo; ndi mnofu wace unabwera monga mnofu wa mwana wamng'ono, nakonzeka."***

**5-Amachidza akhungu.**

Elisa nayenso amachidza akhungu,

# 2-MAFUMU 6:17 ndi 6:20

***"Ndipo Elisa anapemphera, nati, Yehova, mutsegulire maso ace kuti aone. Pamenepo Yehova anamtsegulira maso mnyamatayo, napenya iye.."***

**6-Amaukitsa akufa.**

Eliya ndi Elisa nawonso amaukitsa akufa,

# 1-MAFUMU 17:22

***"Ndipo Yehova anamva mau a Eliya, ndipo moyo wa mwanayo unalowanso mwa iye, nakhalanso moyo."***

# 2-MAFUMU 4:35 ndi 13:21

***"...Ndi mwana anayetsemula kasanu ndi kawiri, natsegula mwanayo maso ace."***

***Chidziwitso:*** Ngakhale Eliya ndi Elisa anali asakuchita zodzizwitsazi kupatula ndi mphamvu ya Mulungu, nayenso Yesu payekha samatha kuchita chinthu zodzizwitsa,

# YOHANE 5:30

***"Sindikhoza kucita kanthu kwa ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza;..."***

**7-Anayenda panyanja.**

Mose inapatulidwa Nyanja kwa iye,

# EKSODO 14:22

***"Ndipo ana a Israyeli analowa pakati pa Nyanja pouma; ndi madziwo anakhala kwa iwo ngati khoma palamanja, ndi palamanzere."***

**8-Amatulutsa ziwanda zoipa.**

Anthu ndi aneneri onyenga nawonso amatulutsa,

## MATEYU 7:22

## *“Ambiri adzati kwa ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m’dzina lanu, ndi m’dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m’dzina lanunso zamphamvu zambiri?”*

**9-Anali munthu mnthawi yomwenso Mulungu.**

Mulibe mBaibulo lonse vesi yomwe ikufotokoza zimenezi.

**10-Atate ndi Yesu ndi amodzi komanso Atate ali mwa iye, ndipo iye mwa Atate.**

Mauwa akhoza kutanthauza kuti uthenga omwe Yesu akulalikira ndi zomwe Mulungu akufuna ndi zimodzi zofanana.

<u>Ena mwa maumboni osonyeza kusiyana pakati pa Mulungu ndi Yesu.</u>

- **YOHANE 14:28**
  ***“Pakuti Atate ali wankulu ndi ine”***

- **MARKO 13:32**

***“Koma za tsiku ilo, kapena nthawi yace sadziwa munthu, angakhale angelo m’mwamba, angakhale Mwana, koma Atate ndiye”***

- **MARKO 10:27**

***“Yesu anawayang’ana iwo nati, Sikutheka ndi anthu, koma zikutheka ndi Mulungu”***

## YOHANE 5:30

***“Sindikhoza kucita kanthu kwa ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza;…”***

- **MATEYU 26:39**

***“Ndipo anamuka patsogolo pang’ono, nagwa nkhope yace pansi napemphera, nati, Atate, ngati nkutheka, cikho ici cindipitirire ine; koma si monga ndifuna ine, koma inu”***

- **MASALMO 121:4**

***“Taonani, wakusunga Israeli sadzaodzera kapena kugona”***

## LUKA 21:37

***“Ndipo usana uli wonse iye analikuphunzitsa m’kacisi; ndi usiku uli wonse amaturuka nagona pa phiri lotchedwa la Azitona”***

**12-Mphamvu zonse zaperekedwa kwa iye. Chili chonse adzafunsidwe Yesu m’dzina lake, adzachichita.**

Ngakhale Yesu anayankhula izi, pali malo ena amene Yesu atafunsidwa kuti alamulire ana awiri a mai wina kuti akakhale ku dzanja lake la manja, ndi wina kulamanzere, muufumu wake **…**

## MATEYU 20:20-23

“***Koma Yesu anayankha nati, inu simudziwa chimene mupempha…sikuli kwanga kupatsa,***

***koma kuli kwa iwo omwe kwakonzedweratu ndi Atate wanga"***

**13-Analenga dziko.**

Izi zikutsutsana ndi mavesi ambiri mBaibulo, ena mwaiwo ndi;

# YESAYA 45:18

***"Pakuti atero Yehova, amene analenga kumwamba , iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi..."***

# YESAYA 43:10

***"...Ine ndine; ndisanakhale Ine, panalibe wolengedwa, ngakhale pambuyo panga sipadzakhala wina."***

**14-Anali pambali pa Mulungu ngati mmisiri.**

# MIYAMBO 8:30 ikuti:

***"Ndinali pa mbali pace ngati mmisiri;"***. oyankhula mu vesiyi sangakhale Yesu chifukwa choti 1. Vesiyi ikupezeka ku Chipangano Chakale. 2. Munthuyi amayankhula zimenezi kwa ana ake pomwe Yesu analibe mwana.

# MIYAMBO 8:32

***"Ndipo tsopano, ananga, mundimvere..."***

Kuonjezera apo, ngati Yesu analenga nawo dziko lapansi, ndiye kuti akuyenera nayenso kudziwa tsiku kapena nthawi yothera dziko. Koma Yesu akuti:

# MARKO 13:32

***"Koma za tsiku ilo, kapena nthawi yace sadziwa munthu, angakhale angelo***

***m'mwamba, angakhale Mwana, koma Atate ndiye"***

**15-Amakhulululuka machimo.**

Anthunso amawakhulululukira adani  ndi amangawa ao ndipo aneneri amadziwitsidwa ndi Mulungu kukhulululukiridwa kwa anthu.

# MATEYU 6:12

## *"Ndipo mutikhulululukire mangawa athu, mongaifenso takhulululukira amangawa athu."*

**GAWO 3**

## MWANA WA MULUNGU?

Umboni wa umwana wa Mulungu wa Yesu.

**1-Yesu wadzitcha kuti ndiMwana wa Mulungu.**

Yesu yemweyo akutinso ochita zabwino ndiana a Mulungu.

# MATEYU 5:44-45

***"Koma ine ndinena kwa inu, kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa kumwamba;..."***

**2-NdiMwana wa Mulungu woyamba.**

Baibulo likutinso Efraimu ndiMwana wa Mulungu woyamba.

# YEREMIYA 31:9

***"...Pakuti ndiri Atate wace wa Israeli, ndipo Efraimu ali mwana wanga woyamba"***

**2-NdiMwana wa Mulungu yemwe anam'bala.**

Baibulo likutinso Davide ndiMwana wa Mulungu yemwe anam'bala.

# MASALMO 2:7

**Mulungu ananena kwa Davide, *"Iwe ndiwe mwana wanga; Ine lero ndakubala"***

**3-Anabadwa popanda bambo, n'chifukwa chake ali mwana wa Mulungu.**

Adamu nayenso anabadwa osati popanda bambo okha, koma ndi mai omwe.

# LUKA 3:38

***"Mwana wa Enosi, mwana wa Seti, mwana wa Adamu, mwana wa Mulungu"***

Mau oti *'Mwana wa Mulungu'* akhoza kutanthauza munthu wachifupi ndi okondedwa ndi Mulungu.

# AROMA 8:14

## *"Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu"*

**<u>GAWO 4</u>**

**MPULUMUTSI YEMWE ANABWERA KUDZAFERA MACHIMO A ANTHU?**

<u>Umboni wa chikhulupirirochi.</u>

**1-Uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa uchimo.**

Ngakhale izi zili chonchi, pali mavesi ochuluka otsutsana ndi chikhulupirirochi.

Yesu akuti amene salandira ufumu wa Mulungu ali oyera kumachimo ngati kamwana sadzalowamo.

# Marko 10:15

***"Ndinthu ndinena ndi inu, Munthu ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse."***

# DEUTRONOMO 24:16

***"Atate asaphedwere ana, ndi ana asaphedwere atate; munthu yense aphedwere tcimo lace lace"***

# EZEKIELI 18:20-21

***"Moyo wocimwawo ndiwo udzafa; mwana sadzasenza mphulupulu za atate wace, ndi atate sadzasenza mphulupulu za mwana cilungamo ca wolungama cidzankhalira ndi coipa ca woipa cidzankhalira. Koma woipayo akabwerera kusiya macimo ace onse adawacita nakasunga malemba anga onse, ndi***

***kicita ciweruzo ndi cilungamo, adzakhala ndi moyo ndithu, sadzafa".***

# GENESIS 5:5

## *"Masiku ace onse anakhala ndi moyo Adamu anali zaka mazana asanu ndi anai, kudza makumi atatu(930); ndipo anamwalira"*

- Kutanthauza kuti ngati Adamu ndi Ava anakhala zaka zochuluka ngati chonchi pambuyo pakuchimwa kwao osafa, ndiye kuti anasiya uchimo wawowo nasatila malamulo ndipo Mulungu adawakhulululukira ndi kusawapatsa chilango cha imfa.

**2-kuti ulandire moyo osatha ulandire iye.**

Malingana ndi Baibulo, chipulumutso ndi moyo osatha umazipeza potsata malamulo a Mulungu.

# MATEYU 19:16-19

# *"Ndipo onani, munthu anadza kwa iye, nati, Mphunzitsi, cabwino nciti ndicite, kuti ndikakhale nao moyo wosatha? Ndipo iye, Undifunsiranji za ca cinthu cabwino? Alipo Mmodzi ndiye wabwino: koma ngati ufuna kulowa m'moyo, sunga malamulo…"*

**3-Anapachikidwa pamtanda.**

Ngati Yesu anapachikidwa pamtanda, ndiye kuti anali otembereredwa ndi Mulungu zomwe sizoona.

# DEUTRONOMO 21:23

# *"Pakuti wopacikidwa pamtengo atembereredwa ndi Mulungu."*

**4-Anabwera kudzafera machimo a anthu.**

- Malingana ndi Baibulo Yesu samafuna kuti agwidwe ndi adani ake naphwedwa.

# MATEYU 26:39

***“Ndipo anamuka patsogolo pang’ono, nagwa nkhope yace pansi napemphera, nati, Atate, ngati nkutheka, cikho ici cindipitirire ine; koma si monga ndifuna ine, koma inu”***

- Kodi Mulumgu ukampempha amayankha kapena samayankha?

# Mateyu 7:7-10

***“Pemphani ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani ndipo mudzapeza; gogodani ndipo cidzatsegulidwa kwa inu. Pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citsegulidwa. Kapena munthu ndani wa inu, amene pompempha mwana wace mkate adzampatsa mwala? Kapena pompmpha nsomba adzampatsa iye njoka kodi?”***

- Tsono ngati Yesu anampempha Mulungu kuti amuteteze kuimfa, Mulunguyo anamyankha Yesu zotani?

# LUKA 22:-43

## *“Ndipo anamuonekera iye mngelo wa kumwamba namlimbikitsa iye.”*

- Ngati mngelo anamlimbikitsa yesu; anamlimbikitsa zoti afa kapena safa?

# AHEBER 5:7

## *“Ameneyo m’masiku athupi lace anapereka mapemphero ndi mapembedzero pamodzi ndi kulira kwakukulu ndi misozi kwa iye amene anakhoza kumupulumutsa iye mu imfa, ndipo anamveka popeza anaopa Mulungu.”*

**5-Anauka kwa akufa.**

Ngati yesu anauka kwa akufa pambuyo pakufa*, tsono chizindikiro cha Yesu cha masiku atatu ndi mausiku ake ali mumtima mwa dziko lapansi (Mateyu 12:40)* chikutanthauzanji? Ngakhale patakhala kusiyana kumbali ya kuwerengera kwa masiku atatu ndi mausiku ake amenewa pofananiza ndi Yona yemwenso chizindikiro chake chidali masiku atatu ndi mausiku ake ali mmimba mwa chinsomba, koma chinthu chimene chili chodziwika bwino n’chakuti Yona anamezedwa ndi chinsomba ali wamoyo, anakhala mmimba mwake ali ndi moyo, ndipo analavulidwa pamtunda ali ndi moyo. Zomwe zikutanthauza kuti Yesu nayenso anali chimodzimodzi ndi moyo mmasiku amenewa.

**GAWO 5**

**MNENERI NDI MTUMIKI WA MULUNGU?**

pambuyo posanthula bwino lomwe buku la Baibulo, zikuonekeratu poyera kuti Yesu muzonse zomwe amayankhula, kuchita ndi kulalika sanali china koma mneneri ndi mtumiki wa Mulungu. Mavesi osonyeza pa zimenezi ndiambiri koma ena mwaiwo ndiwotsatirawa;

# MATEYU 21:11

***"Ndipo makamu a anthu anati, uyu ndi mneneri Yesu wa ku Nazarete wa ku Galileya."***

# LUKA 7:16, 24:19

***"Ndipo mantha anagwira onsewo: ndipo analemekeza Mulungu, nanena kuti Mneneri wankulu wauka mwa ife; ndipo Mulungu wadzaceza ndi anthu ace"*** mau oti '***ndipo Mulungu wadzaceza ndi anthu ace***' akupita kwa Mulungu osati Yesu, ndipo akufuna kutanthauza '*Mulungu akulumikidzana nawo kudzera mwa Yesu'.*

# YOHANE 17:3

***"Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Kristu amene munamtuma."***

**MAU OMALIZA**

Zatsimikizika tsopano kuti mau, chikhulupiriro ndi yankho loona ndi lolondola pa funso loti kodi Baibulo liti Yesu anali yani? Anali mneneri ndi mtumiki wa Mulungu, osati mmodzi wa atatu, kapena Mulungu amene, kapena Mwana wa Mulungu (ndi tanthauzo loti ndi mwana weniweni wa Mulungu osati mongobwerekera chabe) kapenanso mpulumutsi wakufera machimo a athu.

Mmenemu ndi mmenenso Asilamu amamunkhulupirira Yesu; ndimwana wa mwamuna wa Maria, Mesia ndi Mtumiki wa Mulungu. Ndi nzimu wa Mulungu umene anaulenga (ngati nzimu ulionse) ndimau ake amene anayankhulira kwa Maria kuti 'Khala (kutanthauza ndi pakati) ndipo anakhala ndi pakati pa Yesu –mtendere ndi madalitso za Mulungu zipite kwa iye-.

SHARE Islam